Kodi Zikusiyana Pati?

Kodi mungatchule zinthu zitatu zimene zikusiyana pakati pa chithunzi A ndi chithunzi B? Lembani mayankho anu m'mizere ili m'munsiyi, ndipo malizitsani zithunzizi pozikongoletsa ndi chekeni. ZOKUTHANDIZANI: Werengani Ekisodo 25:10-22.

1.....

2.....

3.....

4. **Kodi chithunzi cholondola n'chiti, A kapena B?**





KAMBIRANANI: **Kodi likasa linkaimira chiyani kwa Aisiraeli?** ZOKUTHANDIZANI: Werengani Ekisodo 25:22; Levitiko 16:2. **Kodi n'chiyani chinali chofunika kwambiri kuposa likasalo?** ZOKUTHANDIZANI: Werengani Yoswa 7:1-6, 11, 12. **Ngati mukufuna kukondweretsa makolo anu ndi Yehova, kodi n'chifukwa chiyani muyenera kukhala omvera?** ZOKUTHANDIZANI: Werengani 1 Samueli 15:22, 23; Aefeso 6:1-3.

ZOTI BANJA LICHITIRE PAMODZI: **Munthu aliyense m'banja mwanu afufuze zinthu zosiyanasiyana zokhudza likasa la pangano. Kenako mukumane pamodzi n'kukambirana zimene mwapeza. Mwachitsanzo, kodi patapita nthawi mu likasamo ankasungamo chiyani? Jambulani zinthuzo ndipo kambiranani kufunika kwake.** ZOKUTHANDIZANI: Werengani Aheberi 9:4. **Kodi likasa linkayenera kunyamulidwa bwanji? Kodi chinachitika n'chiyani Davide atalephera kutsatira malangizo amene Yehova anapereka onyamulira likasa?** ZOKUTHANDIZANI: Werengani Ekisodo 37:5; 1 Mbiri 13:7, 9-14; 15:12-15.

1. Zitsulo zonyamuliira. **2.** Mapiko a Akerubi. **3.** Nkhope za akerubi. **4.** B.

www.jw.org © 2011 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania